

**Thunthu La Moyo**  
 Kuzindikira Tsinde La Kuphunzira Kozama

**Zolinga za Moyo**

Paul J. Bucknell #5  
 Rodrick Banda (trans.) www.bffbible.org

1

---

---

---

---

---

---

---

---

**Thunthu La Moyo**

Kuzindikira Thunthu La Moyo

Kuyamikira Thunthu La Moyo

Kukhala Thunthu La Moyo

Kukwaniritsa Thunthu La Moyo

2

---

---

---

---

---


---

---

---

**Thunthu La Moyo** #5

**Zolinga za Moyo**



Mzimu Woyera ndiye moyo wauzimu mkati mwathu

- Mphamvu iliyonse imalowera kwina kwake komanso imakhala ndi kulimbika kwina kwake.
- Moyo wathu wauzimu uli ndi mphamvu yakeyake komanso cholinga chake

- Pamene tikuzindikira zolinga za Mulungu ndikugwirizana ndi Mzimu Woyera, pamenepo tidzayenda mwamphamvu.
- Kodi mudamvapo chipambano champhamvu mmbuyomu?

3

---

---

---

---

---

---

---

---

**Thunthu La Moyo** #5

**Kukulitsa Chidziwitso Chathu**

- Nkhondo zambiri zauzimu zikadatha tikadakhala ndi mayang'aniridwe oyenera.
- Wokhulupirira ambiri sadziwa zolinga za Mulungu pa moyo wao.
- Pamene tamvetsetsa ntchito ya Mzimu, timasintha mmene timawonera zinthu!

"Ndipo Elisa anapemphera, nati, "Yehova, mumtsegulire maso ake kuti aone." Pamenepo Yehova anamtsegulira maso mnyamatayo, napenya iye, ndipo tawonani, paphiripo panadzala ndi akavalo ndi magaleta a moto akumzinga Elisa" (2 Mafumu 6:17).

4

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

5

### Mphepo Ikuwomba

- Sitingamuwone Mzimu koma timadziwa zolinga zake.



“Amene timlalikira ife, ndikuchenjeza munthu aliyense ndikuphunzitsa munthu aliyense mu nzeru zonse, kuti tionetsere munthu aliyense wamphumphu mwa Khristu” (Akolose 1:28).

- ‘Amphumphu mwa Khristu’ ndi ‘oyera’ ndi zolinga zathu ziwiri chabe zikuluzikulu.

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

6

### Mphepo Ikuwomba (2/2)

“Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi zonse; ndiye Mzimu wa choonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona lye, kapena kumzindikira lye. Inu mumzindikira lye; chifukwa akhala ndi inu, nadzakhala mwa inu” (Yohane 14:16-17).

- Mulungu amakhala mwa ife kuti alimbikitse chidziwitso chathu chauzimu.
- Kuti alumikizane nafe.
- Kuti akwaniritse zolinga zake zaulemerero kudzera mwa ife.

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

7

### Mau Otsiriza

- ‘Mphamvu ya moyo wauzimu’ imafaniziridwa ndi ‘mphamvu ya moyo wathupi’ poyendetsa matupi athu a umunthuwa.
- Mmene mphamvu ya moyo wauzimu imagwirira ntchito ndichimodzimodzi mmene Khristu amagwirira ntchito mwa ife kudzera mwa Mzimu Woyera.
- Kuphatikiza pamodzi mwadaladala zofuna zathu ndi zolinga za Mulungu zimaphweketsa moyo wauzimu komanso kukhala moyo wachindunji.

---

---

---

---

---

---

---

---

# Thunthu La Moyo

Kuzindikira Tsinde La Kuphunzira Kozama

# Kufunafuna Malangizo

8

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

9

### Kufunafuna Malangizo

- Mulungu amakhala moyo ochitachita mwa ife kuti atithandizire kuti tikhale moyo wofanana ndi Khristu.
- Woyipayo amagwira ntchito mowirikiza kuti atisokoneze.
- Wokhulupirira amasokonezeka kwambiri pokhudzana ndi mmene akhoza kumakulira.
- Sityika chiyembekezo chathu pa mwana wakhanda.




---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

10

### Fanizo la Thupi

- Yohane adatithandiza kuti timvetsetse kupezeka ndiponso mtundu wa moyo wauzimu poufanizira ndi moyo wa thupi.
- Kufanizira kofunikiraku kumafotokozera momveka bwino kakulidwe ka moyo wathu wauzimu.
- Ganizirani zakuthupi kuti mumvetsetse zauzimu.
- Zobisikazo zimamvetsetseka bwino pamene tilingalira kwambiri pa magawo atatu a moyo wauzimu.

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

11

### 1 Yohane 2:12-14

Ndikulemberani, **tiana**, popeza machimo adakhululukidwa kwa inu mwa dzina lake. Ndikulemberani, **atate**, popeza mwamzindikira lye amene ali kuyambira pachiyambi. Ndikulemberani, **anyamata**, popeza mwamlaka woyipayo. Ndakulemberani, **ana**, popeza mwazindikira Atate. Ndakulemberani, **atate**, popeza mwamzindikira lye amene ali kuyambira pachiyambi. Ndakulemberani, **anyamata**, popeza muli amphamvu, ndi Mau a Mulungu akhala mwa inu, ndipo mwamlaka woipayo (1 Yohane 2:12-14).

- Kodi muli otsimikizika mtima kuti sakufotokoza za magulu a thupi?

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

12

### Magawo Atatu Wokha

- Cholinga ndichokhala ofanana ndi Yesu – wokhulupirira wokhwima.
- Gawo lililonse limafotokozera chimene chimachitika pa gawo lililonse la makulidwe.
- Monga okhwulupirira akuluakulu tikhoza kuthandizira ndondomeko yopita patsogoloyi (e.g. makolo)
- Mabvuto a kukhala ndi mpingo wofoka amachokera kukusaphunzitsa ana athu a uzimu!

Magawo atatu a kukula muuzimu



Kukula kwathunthu kwa Mkhristu	
Wokhulupirira wokhwima (atate)	
Wokhulupirira wamng'ono (mnyamata wachisodzera)	
Wokhulupirira watsopano (mwana)	

---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

13

### Mau Otsiriza

- Makulidwe a uzimu a munthu wokhulupirira amafanana ndi makulidwe a thupi a munthu.
- Kufooka mumpingo sikutengera kusoweka kwa mphamvu ya Uthenga Wabwino kapena Mau a Mulungu, koma kulephera kwa anthu a Mulungu kuti aphunzitse anthu owazungulira moyenera.
- Pali magawo atatu a kukula muuzimu: wokhulupirira atsopano (ana), wokhulupirira achisodzera (anyamata) komanso wokhulupirira wokhwima (atate).

---

---

---

---

---

---

---

---

# Thunthu La Moyo

Kuzindikira Tsinde La Kuphunzira Kozama

## Chidwi

14

---

---

---

---

---

---

---


---

## Thunthu La Moyo #5

15

### Chidwi

- Kodi pondiyenera ndi pati?
- Monga chithunzi cha gulu! Ine ndili pati? Kodi ndikuwoneka ngati chani?
- Chitsanzo cha banja chimamveka bwino kwa wokhulupirira onse konsekonse!
- Magawowa atisunthe ife mmalo mwakuti tipikisane nawo!



---

---

---

---

---

---

---

---

## Thunthu La Moyo #5

16

### Masomphenya Atsopano a Kukula

- Wokhulupirira ambiri amapezeka kuti sakula mmoyo wao wauzimu.
- Ali ndi zobvuta mdela limodzi kapena madela angapo a moyo wao – opanda chiyembekezo.
- “Kukula kwamphamvu” kwa moyo wa thupi ndi wauzimu

Mzimu Woyera akadantengerabe kukukula kwathunthu mmoyo wauzimu.
lilili, Kodi ndipati pamene ndatengera njira yolakwika?
Mulungu ali ndi chikonzero ndi moyo wanga.
Mulungu wandipatsa kuthekera kwakuti ndikule kufikira ndikhwime.
Kodi ndili pati?
Kodi kenaka ndichite chani kuti ndikule?
Ndichite chiyani kuti ndikulebe?

---

---

---

---

---

---

---

---

### Chiyembekezo Chokula

- “Mukutanthauza kuti mukufuna kufanana ndi Yesu?”
- “Kenako ndichite chani?”
- Moyo umadkula mwa iwo wokha.
- Koma tikhoza kuusamalira.

“Tumizani kuunika kwanu ndi choonadi chanu zinditsogolere; Zindifikitse ku phiri lanu loyera, kumene mukhala Inuko. Kuti ndipite kufikira guwa la nsembe la Mulungu, Kufikira Mulungu wa chimwemwe change chenicheni; Ndi kuti ndikuyamikeni ndi zeze, Mulungu, Mulungu wanga” (Masalimo 43:3-4).




---

---

---

---

---

---

---

---

### Mau Otsiriza

- Kukula mokwinimbira kumadziwika ndi kusoweka kwa chilakolako chokula, kapena chikhulupiro chakuti kukula nkosafunikiranso kapena sikoyenera.
- Ngati wokhulupirira awona kuti nkutheka kukula, chidwi chao cha kukula chimayambiranso.

---

---

---

---

---

---

---

---

### Zoyenera Kuti Tichite

- ➔ Kodi pa 1 Yohane 2:12-14 pali magulu ati? Fotokozerani kusiyana kwa mtundu umodzi kwa gulu lililonse pa gawo lililonse, kuthupi komanso kuuzimu.
- ➔ Kodi mukudziwa aliyense amene akuphunzitsidwa kuti akhale wophunzira wa Yesu? Ngati simukudziwapo aliyense, inu mukuganiza kuti zimenezi zikutheka bwanji?
- ➔ Kodi anthu amene mumakhala nawo pafupi ali ndi chidwi chofuna kuphunzira Mau a Mulungu? Fotokozerani.
- ➔ Nanga inuyo changu chanu ndichotani pankhani yophunzira ndi kukula?

---

---

---

---

---

---

---

---

Thunthu La Moyo  
Kuzindikira Tsinde La Kuphunzira Kozama

# Zolinga za Moyo

Paul J. Bucknell #5  
Rodrick Banda (trans.) www.bffbible.org

---

---

---

---

---

---

---

---